


Nowa ndi madzi amphamvu osefukila

Nthano yochokera mu mau a Mulungu, Baibulo,

opezeka mu

*Genesis 6-10*

"Polowela pa mau anu pamapasa kuwala."
Masalimo 119:130

Yolembedwa ndi Edward Hughes
Yojambulidwa ndi Byron Unger; Lazarus

Yotathauzidwa ndi Phiri Williams
Yotengedwa ndi M. Maillot; Tammy S.

Nthano 3 ya zili 60

**M1914.org**

**Bible for Children, PO Box 3, Winnipeg MB  R3C 2G1  Canada**

Chilolezo: Muli ndi ufulu wotenga ndi kuchurukitsa makopewa koma osagulitsa.






















**Mulungu adziwa** kuti timachita zinthu zoipa, zimene zimachedwa chimo. Chilango chauchimo ndi infa.

**Mulungu amatikonda** kwambiri kotero anatuma mwana wake, Yesu, kutifera pamtanda ndi kulipila chilango. **Yesu anadza wamoyo** ndipo anabwereranso kumwamba wamoyo! Ndipo Mulungu angathe kutikhululukira machimo.

**Ngati mufuna kulapa machimo anu,** nenani izi kwa Mulungu: Mulungu wanga wokondedwa, ndikhulupilira Yesu anandifera ndipo alinso ndi moyo. Chonde lowani mumoyo wanga ndi kundi khululukira ma chimo anga, kuti ndikhale ndi moyo wosatha tsopano, ndipo mukhale ndi ine kwa nthawi zonse. Ndithandizeni kuti ndikhale mwa inu ngati mwana wanu. Amen. Yohane 3:16

**Werenga Baibulo ndikuyankhula ndi Mulungu matsiku onse!**

Chichewa


Mulungu anamuchenjeza Nowa kuti kudzakhala chigumula cha madzi ndikukwanila dziko lonse lapansi.
3
"Manga chombo, ngalawa yaikulu yokwanila banja lako ndi nyama zambiri," ndipo Nowa analangizidwa. Ndipo Mulungu anampatsa Nowa malangizo wowonjezera. Nowa anatangwanika kwabasi!
4
Ndipo anthu anamuseka Nowa monyoza kuti chifukwa chiyani ukupanga chombo.
Koma Nowa sanasiye kupanga chombo. Iye anapitiliza kuwauza anthu za Mulungu. Koma panalibe omvera.
5
Nowa anali ndi chikhulupiliro chachikulu.
6
Anakhulupirila Mulungu ngakhale madzi otero sanayambe abwelapo. Posatenga nthawi chombo chinakhala chokhonzeka kutenga zinthu.
7
Kenaka nyama zinabwera. Mulungu anabweretsa mitundu isanu ndiziwiri zamtundu wina, ziwiri za mtundu wina mbalame zazikulu ndi zazin'gono, ...
8
... zilombo zazin'gono ndi zazikulu zinapezeka kulowa muchombo.
9
Ngakhale anthu anamseka namnyozera Nowa pomwe ama lowetsa nyama. Anthu sanasiye kumuchimwira Mulungu. Iwo sanampemphe kulowa nawo mchombo.
10
Pomaliza, nyama zonse ndi mbalame zinalowa. "Lowani mchombo," Mulungu adawa itana. "Iweyo ndi banja lako basi."
11
Nowa, mkazi wake, ana ake atatu ndi akazi ake analowa mchombo. Kenaka Mulungu anatseka chitseko!
12
Kenaka mvula inabwela. Thamanda lodabwitsa linabwera padziko lapansi kwa masiku makhumi anayi ndi usiku.
13
Chigumula cha madzi chinagwa kumizinda ndi kumidzi. Pamene mvula inasiya, ngakhale mapiri anali odzala ndi madzi. China chilichonse chopuma chinafa.
14
Pamene madzi anakwera, chombo chidayandama pamwamba. Mwina munali mudima mkati mwa chombo, mwina mabampu, mwinanso kuopsya. Koma chombo chinamvundikira Nowa kuchigumula.
15
Patatha masiku asanu achigumula, Mulungu anatumiza mphepo yowumitsa madzi.
16
Pan'gono pan'gono chombo chinabwera ndikukhala pamwamba pa mapiri a Ararat. Ndipo Nowa anakhala mkati mwa chombo kwa masiku makhumi anayi pomwe madzi amaphwa.
17
Ndipo Nowa anatumidza makungubwi ndi nkunda kuchoka mchombo paka dzenera kakan'gono anatsegura. Sanapeze malo owuma kuti apume, kenako nkunda inabwelera kwa Nowa.
18